

## SAMBANYENJE PRIMARY SCHOOL EXAMINATION BOARD



### 2022 STANDARD 6 MAYESO A CHIGAWO CHOYAMBA

CHICHEWA (100 Marks)

**Date:**

**Time: 08:00 – 10:00(2hrs)**

#### **Malangizo:**

- *Lembani dzina lanu*
- *Yankhani mafunso*

#### **GAWO A (30 MALIKISI)**

##### 1. CHIMANGIRIZO

Lembani chimangirizo pa mutu uwu; “BOMA LATHU”. Mawu a chimangirizo chanu asachepere 100 komanso kubzola 150. Tsatani izi polemba chimangirizo chanu:

##### Ndime yoyamba

- Tchulani dzina la boma lakwanu
- Tchulani chigawo chomwe bomali limapezeka.

##### Ndime yachiwiri

- Fotokozani mitundu ya anthu ndi ziyankhulo za anthu a m’boma lakwanu.
- Fotokozani mitundu ya magule amene anthu a m’bomali amakonda kuvina
- Fotokozani njira zomwe anthu a m’bomali amapezera ndalama.

##### Ndime yachitatu

- Fotokozani mavuto omwe anthu a m’bomali amakomana nawo.
- Fotokozani momwe mavutowa angathetsedwere

---

---

---

---

---

DZINA LA OPHUNZIRA: \_\_\_\_\_

Lined writing area consisting of 30 horizontal lines.

**GAWO B: KUNVETSA NKHANI(20MALIKISI)**

2. Werengani nkhani yotsatirayi motsamala ndikuyankha mafunso otsatirawo.

Madzi ndi moyo. Mawuwa amanenedwa chifukwa chakuti zachilengedwe zambiri zimadalira madzi kuti zikhale ndi moyo.

Anthu, nyama mitengo ndi zolengedwa zina zimafuna madzi. Munthu amafuna madzi pa zifukwa zosiyanasiyana. Mwachitsanzo, munthu akanva ludzu amamwa madzi chifukwa m’thupi mwake mumafunika madzi. Choncho ndibwinomkumwa madzi aukhondo pafupipafupi kuti akhale ndi moyo wabwino ndi wa zitho. Anthu akafuna kusamba, kuchapa zovala, kuphika kapena kusuka ziwiya zapakhomo amagwiritsanso ntchito madzi.

Madzi amapezeka m’misinje, m’nyanja, m’zitsime ndi m’zithaphwi. Makono anthu amagwiritsa ntchito madzi a pamjigo ndi a mpopi. Kawirikawiri madzi omwe timatunga m’ malo oterewa sakhala abwino kwenikweni. Tsopano popeza madzi ndi moyo, n’kofunika kusamalira kwambiri madziwa.

**Mafunso**

a. Tchulani kufunika kutatu kwa madzi pa moyo wa munthu.

i. \_\_\_\_\_

ii. \_\_\_\_\_

iii. \_\_\_\_\_ (3malikisi)

b. Kodi mawu akuti “zitho” akutanthauzANJI munkhaniyi?

\_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_ (3malikisi)

c. N’chifukwa chiyani anthu ogwira ntchito kumafakitole asamataye zinyalala ndi mafuta m’nyanja?

\_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_ ( )

d. Perekani njira ziwiri mene tingasamalire zitsime zathu.

i. \_\_\_\_\_

ii. \_\_\_\_\_ (6malikisi)

DZINA LA OPHUNZIRA: \_\_\_\_\_

- e. Fotokozani njira zitatu momwe tingasamalire madzi omwe tatunga kumtsinje kapena kuchitsime.
- i. \_\_\_\_\_
- ii. \_\_\_\_\_
- iii. \_\_\_\_\_ (6malikisi)
- f. Kodi mawu oti ‘madzi ndi moyo’ akutanthauzani munkhaniyi?
- \_\_\_\_\_
- g. Perekani mutu wa nkhaniyi.
- \_\_\_\_\_

**GAWO C: (50MALIKISI)**

3. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu otsatirawa.
- a. Zikhulupiro
- \_\_\_\_\_ (2malikisi)
- b. Chilala
- \_\_\_\_\_ (2malikisi)
- c. M’gonero
- \_\_\_\_\_ (2malikisi)
- d. Muvi
- \_\_\_\_\_ (2malikisi)
- e. Chilengedwe
- \_\_\_\_\_ (2malikisi)

Tsekani mzere kungsi kwa mayina a zinthu zosakhuzika m’ziganizo (10 malikisi)

- a. Amayi ali ndi chikondi chachikulu pa mwana wawo.
- b. Mfumu Solomoni adapempha mzeru zochuluka.
- c. Mwanayu akusowa chisamaliro cha mayi ake.
- d. Wantchiyo uja akuchita ulesi.
- e. Pali chidani chachikulu pakati pa Mariya ndi Rute.

DZINA LA OPHUNZIRA: \_\_\_\_\_

Perekani matanthauzo a ndagi zotsatirazi

- a. Chiputu zuu, mbewa laka. \_\_\_\_\_ (2malikisi)
- b. Chimunda change chachikulu koma pokolola ndi m’manja. \_\_\_\_\_ (2malikisi)
- c. Diwa la m’senjere kugwaigwa. \_\_\_\_\_ (2malikisi)
- d. Suzi ndi kuphomphe. \_\_\_\_\_ (2malikisi)
- e. Saopa dziwa. \_\_\_\_\_ (2malikisi)

Perekani zambiri za chimodzi cha mawu otsatirawa.

- a. Ukhondo: \_\_\_\_\_ (2malikisi)
- b. Dzenje: \_\_\_\_\_ (2malikisi)
- c. Venda: \_\_\_\_\_ (2malikisi)
- d. Ntchentche: \_\_\_\_\_ (2malikisi)
- e. Nthenda: \_\_\_\_\_ (2malikisi)

Ikani zizindikiro zam’kalembedwe zoyenera m’ziganizo zotsatirazi.

- a. Chipanda chalowa mchala (2malikisi)
- b. Kodi uve ndiwabwino (2malikisi)
- c. Tiyeni titsamale malo athu (2malikisi)
- d. Atate amayi ndi mwana wakhanda akutsekula m’mimba. (2malikisi)
- e. mmizinda muli ukhondo (2malikisi)

**MAFUNSO ATHERA PANO**